



Khisisimisi ndi
Nyengo ya Pasaka
- Zitanthauza Chiyani?



Ilembedwa ndi JOHN R. CROSS
zithunzi zidajambulidwa ndi MATT ALMY
lomasuliridwa m'Chichewa ndi RODRICK BANDA



Khisimisi ndi Nyengo ya Pasaka - Zitanthauza Chiyani?

Timapeza yankho lafunso limeneli m'buku limodzi lokha – buku lalikulu lotchedwa 'Baibulo' kapena kuti 'Buku Lopatulika'.

Liwu lakuti *Baibulo* ndi lakalekale, limene limatanthauza kuti 'buku'.

Liwu lakuti *lopatulika* limatanthawuza kuti "palibenso lina lofanana nalo'.

Tikamakamba za Baibulo, timakamba za Buku Lopatulika, limene palibenso lina lofanana nalo. Palibenso mabuku ena amene akhoza kufanana ndi Baibulo. Ilitu ndi Buku Lopatulika.

Baibulo limakamba za milungu yambiri, koma ndi Mulungu m'odzi yekha mwa milungu imeneyi amene amatchedwa 'woyera'. Mulungu ameneyu ndi wosiyana ndi milungu ina yonse. Iye ndi wapaderadera. Iyeyu ali wosiyana ndi ena onse.

Anthu amakhala ndi mayina monga Tadala, Tiyamike, Chiyembekezo kapena Mphatso. Chimodzimidzinso Mulungu ali ndi dzina. Dzina lake ndi Yahweh.

Popeza Yahweh ndi Mulungu wosiyana ndi milungu ina anthu a kale adaleka kugwiritsa ntchito dzinali. M'malo mwake, adamutcha Ambuye. Dzina limeneli ndi limene anthu amapatsa munthu wofunikira kwambiri – munthu amene ali ndi ulamuliro. Ngakhale Ambuye Yahweh ndi Mulungu wamkulu, Iye amafuna akhale pa ubwenzi ndi anthu. Iyeyu amafuna ife titamudziwitsitsa ndithu.

Chifukwa cha chimenechi Mulungu adatipatsa Baibulo. Imeneyi ndi kalata yofunikira kwambiri, imene Yahweh adatilemba ife tonse.

Yahweh adalemba kalata imeneyi zaka zambirimbi zapitazo. Komabe, uthenga umene ulimkalata imeneyi ndi wofunika kwambiri kwa ife lero lino monga momwe udalili nthawi imene idalembedwera. Ife tonse timayenera kudziwa zimene Baibulo limanena kwa ife. Tikamawerenga kalata yapaderaderayi, timazindikira tanhawuzo la Khisimisi ndiponso Nyengo ya Pasaka.

Ndime zoyambirira za m'Baibulo zimatiwuzira kuti Yahweh sadachite kubadwa ndiponso sadzafa.¹ Yahweh alibe chiyambi ndiponso alibe mathero ake. Mulungu ameneyu adalipo kunthawi zosayamba ndipo adzakhalapo mpaka muyaya. Ichi ndi chimodzi mwa zinthu zimene zimamupangitsa kuti akhale wapaderadera – ndipo palibe wofanana naye.

Baibulo limanena kuti, pachiyambi, kudali Mulungu yekha. Kudalibe zomera, nyama, ngakhale anthu.



Kudalibenso dziko lapansi, mwezi kapena dzuwa Kudalibenso milungu ina. Kudalibe chilichonse!


Ambuye Yahweh yekha ndiye adalipo kuyambira pachiyambi.

Baibulo limatiwuzira kuti Mulungu adalenga zinthu zonse zowoneka ndi maso ndiponso zinthu zonse zosawoneka.

Chimodzi mwa zinthu zimene Yahweh adazilenga moyambirira ndi angelo. Ifetu sitingawawone angelo, monganso sitingamuwone Mulungu. Angelo ndiponso Mulungu ndi mizimu. Onse ndi wofanana ndi anthu, chifukwa amaganiza komanso amatha kupanga chiganizo; komabe alibe matupi a nyama ndi mafupa.

Ngakhale angelo ali mizimu, iwowatu similungu ayi. Iwo safanana ndi Yahweh. Mulungu adalenga angelo kuti akhale atumiki ake opatulika. Iwowa adalengedwa kuti azichita zinthu zonse zimene Yahweh wawalamulira.

Angelo onse ankangowonerera ndi kumayimba nyimbo pamene Mulungu anakalenga dziko.



Baibulo limatiwuzwa kuti pamene Mulungu *ankalenga* dziko, adalilenga modabwitsa kwambiri. Iye tikamapanga zinthu, timafuna tikhale ndi zipangizo monga dothi ndi madzi. Nthawi zina timagwiritsanso ntchito mitengo, misomali ndi zomatira.

Komabe, Baibulo limatiwuzanso kuti pamene Mulungu *ankalenga* dziko, sadagwiritse ntchito zipangizo zili zonse. Mulungu adangonena mawu – ndipo dziko lidalengedwa!


Mulungu adati, “Kuwale!” Ndipo nthawi yomweyo kudawala ndipo mdima udathawa.

Yahweh adalenga zinthu zonse mwakungoyankhula ndi pakamwa pake. Mulungu ndi wamphamvu kwambiri – akhoza kuchita chilichonse! Palibenso akhoza kufanana naye! Iye ndi woyerayera.

Baibulo limatiwuzwa kuti Mulungu adalenga dzuwa, mwezi ndi nyenyezi. Iye adaziyyika zimenezi mumlengalenga pamalo pamene adafuna kuti zizikhala. Mulungu adachita izi popeza Iyeyo amapezeka paliponse.

Ndikwabwino kudziwa kuti Mulungu ali ponseponse. Iye ali ndi inu, alinso ndi a pabanja anu komanso nthawi yomweyo ali ndi anzanu onse. Mulungu ali ndi onsewo ngakhale atapita kutali kwambiri, kapena amakhala kumene aliliko.

Popeza Yahweh amapezeka paliponse nthawi imodzi yomweyo, Iyeyu amadziwanso zimene tikuganiza. Iye amadziwa ndiponso amazindikira zinthu zonse. Iye sitingamubisalire Mulungu.



Tikawona zinthu zimene Yahweh adazilenga, ife timawona ukulu wake wa Ambuye Mulungu.

Baibulo limatiwuzwa kuti Mulungu adalenga dziko kwa masiku asanu ndi limodzi. Ndi Ambuye Yahweh yekha amene akhoza kuchita izi.

Mulungu adalenga zakudya zimene timadya, mpweya umene timapuma komanso madzi amene timamwa.

Iye adalenga mitsinje, nyanja ndi mapiri. Mulungu adalenga mitengo yonse ndi maluwa wonse.

Mulungu adalenga nsomba zimene zimasambira m’nyanja, komanso mbalame zimene zimawuluka mumlengalenga. Iye adalenganso nyama zimene zimakhala kuthengo ngakhalsenso zimene zimawetedwa.

Potsiriza, Mulungu adalenga anthu – mwamuna ndi mkazi. Ambuye adawakonda anthuwa ndipo ankawasamalira bwino.

Iye adapanga munda wangwiro. Mulungu adawudzaza ndi mitundu yonse ya mitengo, maluwa ndi nyama zoweta. Iye adachita izi chifukwa cha anthuwa. Mulungu adafunitsitsa kuti anthuwa asangalale ndi zinthu zonse zimene Iye adazilenga.

Tikawona kudabwitsa kwa dziko limene Mulungu adalenga, tikhoza kuwona kuti Yahweh ndi wamphamvu kwambiri. Iye amadziwa machitidwe a zinthu. Ndi Mulungu wamkulu yekhayu amene akadakhosha kulenga dziko limene ife timakhalamo.

Popeza Ambuye Yahweh adalenga zinthu zonse, Iyeyu ndiye mwini wake wa zonse. Zinthu zimene inu mwapanga zimakhala zanuzanu chifukwa inu mudazipanga nokha. Izi zili chimodzimodzi ndi Mulungu. Chifukwa chakuti Mulungu adalenga zinthu zonse, zonsezo ndi zake za Iye mwini. Chifukwa cha chimenechi Yahweh, timamutcha kuti ndi Ambuye. Izi zimatanthawuza kuti Iye ndiye Mfumu ndipo kuti zinthu zonse zimene adazilenga ndi zake.

Mulungu adazilenga, ndipo zonse ndi zake.

Baibulo limati Yahweh ndi wabwino ndi wachifundo chosatha.

Tangowonani zinthu zokongola zimene Ambuye adalenga. Kukadathekatu Mulungu kulenga maluwa onse kuti akhale akuda ndi woyera, koma m'malo mwake Iye adawalenga wokongola ndiponso a mitundumitundu.

Mulungu akadatha kupanga chakudya choyipa kwambiri. M'malo mwake, Iye adachipanga kuti chikhale chokoma pakuchidya komanso cha fungo labwino. Iye adapanga mitundu yonse ya zipatso ndi maluwa, tizilombo ndi nyama, mawonekedwe ndi mamvekedwe a zinthu – zonsezi adazichita kuti ife tikondwere nazo.

Yahweh adachita zonsezi popeza amatisamalira.


Baibulo limanena kuti Mulungu amatikonda.

Baibulo limatiwuzanso kuti Yahweh amakondwera zinthu zikamachitika momwe ziyenera kuchitikira.

Tangoganizani chisokonezo chimene chikadakhlapo dzuwa likadati lilowe tsiku lina koma osatulukanso kwa masiku atatu. Ndichifukwa chake Mulungu adakhazikitsa malamulo. Iye adakhazikitsa lamulo lokhudzana ndi dzuwa – limayenera kutuluka m'mawa ndi kulowa madzulo. Ndipo limayenera kuchita izi tsiku ndi tsiku osasintha. Mulungu adakhazikitsa malamulo okhudza chinthu chilichonse chimene adachilenga, kuti dziko lizigwira ntchito yake m'njira yoyenera.

Mulungu adapanganso malamulo akuti anthu azitsatira. Nthawi zina sitikondwera ndi malamulo. Komabe, taganizani mofatsa kuti kodi dziko likadakhala lotani popanda malamulo. Kuyendetsa galimoto kukadakhala kowopsa ngati kukadakhala kopanda zikwangwani za pa msewu. Popanda malamulo wotidziwitsa mbali ya msewu imene tiziyendamo, aliyense akadamasowa chochita. Popanda malamulo, miyoyo yathu ikadakhala yovuta.

Ambuye Mulungu adapanga malamulo chifukwa amadziwa zinthu zotiyenera. Iye amadziwa kuti zinthu zikamachitika moyenera, timakhala anthu achimwemwe ndi wotetezedwa. Iyi ndi imodzi mwa njira zimene Yahweh amawonetsera chikondi chake kwa ife.




Baibulo limanena kuti Mulungu adalenga dziko. Ndipo zinthu zonse zinali zangwiro – padalibe choyipa chilichonse. Lidali dziko labwino pa china chilichonse. Ambuye Yahweh adalenga dziko langwiro, chifukwa Iyeyo ndi wangwiro. Iye sachita choyipa chilichonse. Iyeyu ndi wangwiro.

Kwawo kwa Mulungu ndi kwabwinonso. Kumatchedwa Kumwamba. Baibulo limanena kuti Kumwamba ndikokongola zedi. Kumakhala ngati kumalo kokongola kumene kuli mitengo ndi mtsinje. Ndipo pakatikati pa malo amenewa pali mzinda wokongola, komanso wotetezedwa bwino. Mzinda umenewu ndi wodabwitsa, ndipo Mulungu adakonza misewu ya mumzindawo ndi golide.

Kumwamba kulibe matenda, zowawa kapena imfa. Kulibenso udzu kapena zomera zokhala ndi ululu wakupha. Kumwamba kulibe kanthu kowonongeka kapena kakutha. Kulibenso anthu woyipa kapenda wopanda chifundo ndipo anthu wonse kumeneko amakhala mokondwera. Kumwamba kuli nyimbo zabwino zokhazokha. Nyama zonse zimakhahirana bwino ndi anthu. Kumwamba kulibe kugona, chifukwa kulibe mdima kapena usiku. Tsiku ndi tsiku kumakhala kowala.

Kumwamba ndi kumalo angwiro kumene anthu angwiro ndi angelo angwiro amakhhalako ndi Mulungu wangwiro. Kumwamba ndi kodabwitsa, ndipo nkovuta kufotokozerwa kwake.



Yahweh atatsiriza kulenga dziko langwiro, chinthu china chowopsa chidachitika. Mngelo wofunikira kwambiri pamaso pa Mulungu sadakondwere.

Dzina la mngelo ameneyu linali Lusifala, limene limatanthauza 'Nthanda Yonyezimira.' Mulungu adamulenga mngeloyu kuti azigwira ntchito ya paderadera. Lusifala adayamba kuganiza kuti amayenera kulandira zokoma zoposa pamenepa. Iye sadafune kuti apitirize kukhala mngelo. Iyeyu adafuna kukhala ndi ulamuliro. Lusifala adaganiza kuti nayenso adayenera kukhala Mulungu!

Popeza sadafune kutsatira malamulo a Mulungu, Lusifala adapanga malamulo akeake. Iye adapangira angelo ena ambiri kuti amenye nkhondo yolimbana ndi Yahweh. Iwowa adafuna kuti awononge zinthu zonse, chinthu chimene chidabweretsa chisoni Kumwamba.

Baibulo limagwiritsa ntchito mawu a padera pofuna kufotokozera chisankho chimene Lusifala adasankha chakuti alimbane ndi Mulungu. Baibulo limatcha chinthu chimenechi tchimo. Kuchita tchimo ndiko kupanga chiganizo chosatsatira malamulo a Mulungu. Mukachita tchimo zimakhala ngati mukumuwuzza Mulungu kuti mukuganiza kuti muli ndi nzeru zomuposa Iye. Tchimo limawononga zinthu ndiponso limakhumudwitsa.

Timadziwa kuti izi ndi zowona pamene munthu wina wachita za uchifwamba kapena sadamvere lamulo. Izi zimapweteka anthu ena. Wachifwamba uja akagwidwa, amalandira chilango. Nthawi zina amapereka ndalama kapenanso kumangidwa ndi kupita kundende. Ichi ndicho chilungamo chake. Sichinthu chabwino kuti munthu akachita chinthu cholakwika asalandira chilango.

Chomwechonso, Baibulo limatiwuzza kuti Mulungu ndi wolungama nthawi zonse. Iye sakondwera anthu akamachimwa. Iyeyu amadziwa kuti tchimo limapweteka anthu ena. Ndipo Iyeyu amapereka chilango choyenera malinga ndi tchimo limene munthu walichita. Chilango chake sichikhala chochepa kapena chochulukuka. Yahweh amachita zinthu zabwino ndi zoyenera nthawi zonse.



Lusifala ndi angelo ake sadamukonde Mulungu ndipo sadafune kumumvera Iye. Popeza Yahweh ndi wangwiro, Iye sakadakhala ndi angelo woyipawa m'dziko lake langwiro. Iwowa adali kuwononga Kumwamba. Choncho, Mulungu adawapirikitsa ndi kuwalamulira kuti asadzabwererenso.² Mulungu adasintha dzina la Lusifala ndikumutcha *Satana*, dzina limene limatanthawuza kuti 'mdani'. Satana adasanduka mdani wa Mulungu.

Mulungu adakonza malo atsopano amene Satana ndi angelo woyipawa azikhalako. Chifukwa chakuti angelowa ndi woyipa, malo awo atsopanowa analinso woyipa. Chifukwa chakuti angelowa anali owuma mtima ndi wosowa chimwemwe, malo atsopanowa anali wopweteka ndiponso wosowetsa mtendere. Malo atsopanowa anali owopsa ndipo adatchedwa "Nyanja ya Moto".³

Anthu onse amene amakhala malo amenewa, amakhalako kwamuyaya. Malo amenewa ndi malo amene Satana ndi angelo ake woyipa adzalandirirako chilango.



Angelo ambiri adatsatira Satana nasankha kusamvera Mulungu. Komabe, angelo enanso ambiri adapitiriza kumamvera Mulungu ndiponso kukhala atumiki ake a paderadera. Angelo abwinowa amakhala ndi Mulungu ndi kumutumikira Iye Kumwamba – mudzi wangwiro wa Yahweh.

Baibulo limanena kuti pamene Mulungu adalenga dziko pachiyambi paja, dzikoli lidali ngati Kumwamba. Kudalibe misozi, zowawa kapena mantha. Kudalibe anthu woyipa ndi wopanda chifundo. Kudalibe munthu wakuba, wabodza kapena wakupha. Kudalibe tchimo lamtundu uli onse. Koma koposa zonse, kudalibe chinthu chimene chinkafa.


Dziko limene Mulungu adalenga linali labwino ndi lokoma kukhalamo. Mulungu adafuna zinthu zizikhala chomwechi.

Linali dziko langwiro.

Anthu amene Mulungu adalenga adalinso angwiro. Ndi anthu angwiro wokha amene akhoza kukhala pamodzi ndi Mulungu wangwiro.

Munthu wamwamuna woyamba adatchedwa Adamu ndipo mkazi wake adali Hava. Yahweh adayika anthuwa m'munda wokongola umene Iye adawulenga.

Mulungu adalola Adamu ndi Hava kuti azipita kulikonse kumene akadafuna. Iwo ankadya chilichonse chimene ankafuna, koma chimodzi chokha samayenera kudya. Mulungu adawalamulira kuti asadye chipatso chamtengo umodzi okha.




Ngati Adamu ndi Hava sadamvere lamulo limodzi lokha; ili likadakhala tchimo. Iwo akadasankha kuchita tchimo, sizikadakhala zotheke kuti akakhale pamodzi ndi Yahweh.

Sichidali chinthu chovuta kuti Adamu ndi Hava amvere lamuloli. M'munda muja mudali mitengo yambiri ya zipatso. Komabe, Adamu ndi Hava akadawonetsa kuti amakhulupirira Ambuye Yahweh mwakumumvera Iye. Iwo adakhulupirira kuti Mulungu amadziwa zimene zili zabwino kwa iwo. Izi ndi zimene Mulungu amafuna.

Yahweh ankanena kuti, 'Mundikhulupirire Ine'.

M'menemu ndi m'mene zinthu zidalili pachiyambi – anthu ankakhulupirira Mulungu wangwiro m'dziko langwiro.



Kenaka Satana adabwera m'munda wokongola uja. Iye adawuza Adamu ndi Hava kuti Yahweh ankawabisira chinthu china chake chabwino. Satana adawawuzanso kuti akadzadya chipatso chamumtengo umodziwo, iwo adzakhala ngati Mulungu.⁴



Kodi Satanayu ankanena zowona kapena ankangowanamiza? Kodi Adamu ndi Hava akadachita chiyani? Iwo akadakhulupirira Satana, akadadya chipatsocho. Komabe, iwowa akadakhulupirira Mulungu, sakadadya. Nanga iwowa akadayenera kukhulupirira yani? - Yahweh kapena Satana? Kodi iwowa akadadalira yani?



Adamu ndi Hava adayamba kuganiza kuti nkosakwanira kungokhala anthu angwiro m'munda wangwiro wa Mulungu. Iwowa adafuna kuwonjezerapo zina. Iwo adafuna kufanana ndi Yahweh. Choncho, iwowa adachita chinthu chimodzi, chija Mulungu adawaletsachi - iwo adadya chipatso.

Adamu ndi Hava adakhulupirira bodza la Satana. Iwowa adaganiza kuti adali ndi chidziwitso choposa cha Mulungu pa chinthu chabwino ndi choyenera kwa iwo. Iwo sadamvera lamulo limodzi losavuta la Mulungu, koma adayanjana ndi Satana nayamba kutsutsana ndi Yahweh.

Ili lidali tchimo.

Chifukwa cha tchimo la Adamu ndi Hava, dziko lonse lidasintha. Silidakhalenso dziko lotetezedwa ndi langwiro monga lidalili kale. Kukhala m'dzikomu kudafunika kugwira ntchito molimbika. Udzu udamera m'nthaka. Dziko lidasanduka malo ochititsa mantha. Chifukwa cha tchimo, dziko lidadzaza ndi matenda komanso nkhowa. Dziko lidasanduka malo a imfa.

Adamu ndi Hava adaganiza kuti ankasankha chinthu chabwino.



M'malo mwake chisankho chawo chosamvera Mulungu chidawononga zinthu zonse. Baibulo limanena kuti imfa idalowa m'dziko lapansi chifukwa cha kuchimwa kwa Adamu ndi Hava.

Imfa ndi chinthu choyipa kwambiri. Munthu akafa, mzimu wake umachoka mthupi lake wosabwereranso. Munthu wakufayo sangadzakhalenso ndi moyo pa dziko lapansi. Mnzathu watisiya ndipo timamupukwa - imfa yatilekanitsa.

Chomwechonso, pamene Adamu ndi Hava adakhala kumbali ya Satana, tchimo lawo lidawalekanitsa ndi Yahweh. Ubwenzi udatha, ndipo Adamu ndi Hava adawona kuti adalibe bwenzi. Ichi ndi chimene Baibulo limatanthawuza likamakamba za imfa. Tchimo lidatilekanitsa ndi Mulungu.

Nthawi zonse tchimo limawononga zinthu- lidawononga dziko limene Mulungu adalilenga langwiro. Lidawononganso ubale wapaderadera umene udalipo pakati pa Yahweh ndi Adamu komanso Hava.

Komabe, izi sizidathere pamenepa. Popeza iwowa adalowa m'chijanano ndi Satana, matupi awo akadzafa, iwo adayenera kupita ndi kukakhala kwawo kwa Satana kumene ndi kumalo owopsa. Adamu ndi Hava adayenera kukhala M'nyanja ya Moto ku nthawi za muyaya! Iyi idali nkhani yomvetsa chisoni; Baibulo limanena kuti imeneyi ndi Imfa ya Chiwiri.

Komabe, Mulungu sadafune kuti Adamu ndi Hava akakhale ndi Satana. Mulungu adakonda Adamu ndi Hava, koma iwowa sakadakhala Kumwamba. Ndi anthu angwiro wokha amene akhoza kukhala Kumwamba. Iwo adasankha kuti akhale anthu wochimwa mwakukhulupirira Satana. Nanga Mulungu akadachita chiyani?

Sikutitu Mulungu adalibe yankho! Iye adali nayo ndondomeko. Iye adawuzako pang'ono Adamu ndi Hava ndondomeko yakeyo ndipo uwu udali Uthenga Wabwino kwa iwo.

Mulungu adalonjeza kuti adzatumiza munthu wapaderadera ku dziko lapansi. Baibulo limamutcha



Mpulumutsi. Iye adzatha kupulumutsa Adamu ndi Hava ku chilango chimene adayenera kulandira chifukwa cha tchimo lawo. Iyeyu adzawapulumutsa ku imfa ya chiwiri.

Mulungu sadafotokozere momwe mpulumutsiyu adzapulumutsire Adamu ndi Hava ndikuwapanga iwo kuti akhalenso angwiro. Komabe Iye adalonjeza kuti njira ilipo.

Kodi Adamu ndi Hava akadakhulupirira Mulungu tsopano?

Kodi iwowa akadamudalira Iye?



Ndi chinthu chofunika kwambiri kuzindikira tanthawuzo la mawu akuti 'kudalira'.

Apa mundilole kuti ndifotokozere. Tiyeni ndikuwuzeni kankhani.


Tsiku lina agogo ake a Ndazona adamutenga kupita naye kokayenda m'mbali mwa mtsinje. Ndazona ankayenda m'mbali kwambiri mwa mtsinje uja ndipo adaterereka ndi kugwa. Iye adagwera m'madzi! Ndipo iyeyu adayesetsa kuti akafike kumtunda pamene mafunde ankamukokera kutali. Ndazona adachita mantha akulu. Madzi ankazizira kwambiri. Chifukwa chakuti zovala zake zidanyowa ndikuyamba kulemera, iye adawona ngati wayamba kumira.

Kenaka agogo ake adalowa m'madzi woyendawo. Iwo adali munthu wamphamvu ndipo mapazi awo adaponda molimbika pa nthaka ya pansi pa madzi.

Ndi manja awo ataliatali, agogo aja adamufikira Ndazona, nafuwula, 'Kuno! Gwira dzanja langa, ndikupulumutsa iwe. Ungondidalira!'

Kodi Ndazona adayenera kuchita chiyani? Ngati iye amakhulupirira agogo ake, akadagwira dzanja lawo. Koma ngati samawakhulupirira agogo akewa, Ndazona akadayesetsabe kuti adzipulumutse yekha. Zikadatengera agogo ake kapena iye mwini.

Kodi iyeyu adalire yani?



Ndazona adayandikira ndi kugwira dzanja la agogo ake. Iye adakhulupirira kuti agogo ake akhoza kumupulumutsa kuti asamire m'madzi. Ndazona adapanga chisankho choyenera.

Ndichisankho chotere chimene Mulungu adafuna kuti Adamu ndi Hava apange. Iye adafunitsitsa kuti iwowa amudalire, ndi kukhulupirira kuti Iyeyu akhoza kuwapulumutsa kuchokera kumalo woyipitsitsa kumene ndi kwawo kwa Satana.

Yahweh adali ndi njira yowapulumutsira koma poyamba Adamu ndi Hava adayenera kumudalira Iye.



Ambuye Yahweh sadafotokoze zonse zokhudzana ndi njira yake ya chipulumutso kwa Adamu ndi Hava, komanso sadafotokoze zonse za Mpulumutsi. Komabe, Iye adalonjeza. Ngati anthu adzadalira Mulungu, iwowa akadzafa, Mulungu adzawasandutsa angwiro. Anthu angwiro akhoza kukhala ndi Mulungu Kumwamba. Zimene iwowa amayenera kuchita ndi kudalira Mulungu basi ndi kukhulupirira lonjezano lake. Ndizosavuta chonchi.

Komabe, vuto lalikulu lidalipobe. Mulungu sadakangopanga Adamu ndi Hava kuti akhale angwiro ndi kuwalola kuti akalowe Kumwamba iwowa asadachitepo kanthu za tchimo lawo. Adamu ndi Hava adayanjana ndi Satana ndipo adakhala anthu ochimwa. Mulungu sakadangozikankhira ku nkongo ngati kuti izi sizidachitike. Sizikadakhala zinthu zabwino ndi zoyenera Iye akadakhala ngati tchimo lawo sadalidziwe. Mulungu amayenera kupereka chilango chifukwa cha choyipa chilichonse.

Tsono, kodi Mulungu akadalanga bwanji tchimo la Adamu ndi Hava wosawalanganso iwowa?

Funso limeneli ndilofunika kwambiri. Tawonani, ife tonse tili ngati Adamu ndi Hava. Tili ndi tchimo lofunika chilango. Pakuti tonsefe tidachimwa, tiyenera kuzindikira momwe Mulungu akhoza kulangira tchimolo koma wosalanga anthu.

Pofuna kuti ife timvetsetse izi, Mulungu adapitirizako pang'ono kufotokozerana ndondomeko yake.

Popeza anthu sadamvetsetse kuyipa kwake kwa tchimo, Mulungu adawawuza kuti azichita chinthu china chake kuti mwa chimenechi azindikire kuyipa kwa tchimo. Chimenechi chiwathandizanso kuti adziwe momwe Iye angaperekere chilango kwa tchimo koma wosalanga anthu.

Yahweh adawawuza kuti iwo azisankha nyama – mwanawankhosa. Azikhala mwanawankhosa wamwamuna ndipo asamakhale ndi chilema chilichonse pa thupi lake. Asamakhale ndi matenda aliwonse kapenanso wowulala. Idayenera kukhala nyama yangwiro.

Mulungu adanena kuti mwanawankhosayu azimutengera pa guwa la nsembe, malo a paderadera a imfa. Munthu

amene wabweretsa mwanawankhosayu adayenera kuyika dzanja lake pa mutu pa mwanawankhosayo. Mulungu adati, mwakuchita ichi, kudzakhala ngati kuyika machimo onse a munthuyo pa mwanawankhosayo.

Tsopano chinthu chomvetsa chisoni chidayenera kuchitika.



Kodi mumakumbukira m'mene imfa idabwerera m'dziko lapansi chifukwa cha uchimo? Chabwino, chifukwa chakuti munthu wayika machimo ake pa mwanawankhosa; mwanawankhosayo ankayenera kufa. Izi zidathandiza anthu kuti azindikire kuti uchimo wa munthu udapha nkhosa.

Mulungu adawuza anthu kuti azichita zimenezi ndi cholinga chakuti iwowa amvetsetse ndondomeko yake. Umu ndi m'mene Iye adzaperekera chilango kwa tchimo wosalanga anthu. Mwanawankhosa adalandira chilango m'malo mwa munthu.

Munthu adachita zimene Mulungu adanena chifukwa iye adadalira Yahweh. Iye adakhulupirira kuti mwanawankhosa adalandira chilango chimene chidayenera kugwera munthu.



Nthawi ikadzakwana yakuti munthu afe, Mulungu adzamupanga kuti akhale wangwiro ndi cholinga chakuti akalowe ndi kukhala Kumwamba.

Iyi idali ndondomeko ya Mulungu. Imeneyi ndi imodzi mwa njira zimene Iye akadatsata pofuna kuwonetsera chikondi chachikulu chimene ali nacho pa ife.



Komabe, anthu ena sadakhulupirire ndondomeko ya Mulungu.

Iwo adanena kuti pali milungu ina imene ndi yofunikira kwambiri kuposa Yahweh. Iwo adaganiza kuti milungu imeneyi idali ndi ndondomeko zabwino.

Zimene anthuwa sadazindikire ndi zakuti milungu imeneyi idali angelo woyipa a Satana. Angelowa amangonama kuti adali ngati Yahweh kuti awanyenge iwo. Iwowatu ankanena za bodza ndiponso samanena chowonadi.

Sichidali chinthu chabwino kuti anthu aziganizira kuti angelo oyipawa adali wofunikira kwambiri kuposa Yahweh. Pali Mulungu owona m'modzi yekha ndipo anthu ayenera kumumvera Iye. Yahweh yekha ndi amene amanena zowona.

Ngakhale zinthu zili chomwecho, anthu adatsimikiza mitima yawo kuti ndondomeko za Yahweh sizidali zabwino. Kungoganiza kuti munthu akhoza kukhala wangwiro atangodalira Mulungu chabe - izi adaziwona ngati zophweka kwambiri. Iwo adaganiza kuti kudalinsu koyenera kuti iwo achitepo kanthu kena ndithu, kotero kuti adapanga ndondomeko zawo. Iwo adadzipangira malamulo awoawo.

Iwo adati ngati anthu adachita zinthu zabwino zochuluka koposa zoyipa, ndiye kuti Mulungu akhoza kukondwera. Ngati anthu atakhala achifundo, ndiye kuti akhoza kukhala abwino kwambiri kotero kuti akhoza kuyerekezedwa kukhala Kumwamba.

Kodi inu mukudziwa? Anthu amenewa sadazindikire kuti adayenera kukhala abwino mwamtundu wanji kuti afike pa muyeso wokhala ndi Mulungu Kumwamba kwangwiro.

Motero Ambuye Yahweh adafotokozerapo zina mwa zinthu zimenezi.



Iye adanena kuti ngati anthu adzaba kanthu kalikonse, ngakhale kakang'ono kwambiri, ndiye kuti saliwoyenera Kumwamba.

Yahweh adawawuza kuti ngati iwo adzakhala wokonda ndalama kuposa m'mene azimukondera Iye, ndiye kuti iwowa sali angwiro.

Iye adawawuzanso kuti ngati sangathe kubweza mkwiyo, ndi tchimo ndithu.


Ngati iwo amanena bodza, ngakhale kabodza kakang'ono, ndiye kuti sali angwiro. Kunena zonama ndi tchimo.

Ambuye adanena kuti kukhala wopanda chifundo kapenanso kugwiritsa ntchito dzina la Mulungu mosayenera ndi tchimo.

Kusapereka ulemu kwa abambo kapena amayi awo, ngakhale kamodzi kokha, zimatanthawuza kuti iwo sadali angwiro.

Ndi anthu angwiro okha amene akhoza kukhala pamodzi ndi Mulungu wangwiro.

Mulungu adapereka kwa anthu ake malangizo khumi amene



amatchedwa Malamulo khumi a Mulungu. Ambuye adalemba malamulowa pa miyala iwiri. Padalibe Munthu amene akadakhoza kuwonjezerapo malamulo akeake kapena kuchotsapo ngakhale limodzi. Malamulo a Mulungu sasintha.

Ambuye adapereka miyala iwiri kwa munthu dzina lake Mose. Mose adayenera kuwawonetsa anthu onse zimene Yahweh adalemba.

Aliyense adayenera kuzindikira kuti, ngakhale atayesetsa mwamtundu waji, sangathe kusunga Malamulo onse khumi a Mulungu mwa iwo wokha. Kunali kosatheka kuti iwo akhale abwino ndi woyenera kukhala ndi Mulungu. Iwo adali anthu ochimwa. Iwowa sakadatha kudzipulumutsa ku chilango choyenera tchimo lawo.

Iwo adafunika akhale ndi Mpulumutsi - adafunika akhale ndi mwanawankhosa.

Kwa zaka zambiri, anthu adayembekezera kubwera kwa Mpulumutsi.

Kenaka, tsiku lidafika. Mpulumutsi adafika pa dziko! Chinthu chodabwitsa kwambiri chidali chakuti Yahweh mwini wake ndiye adali Mpulumutsi. Inde ndi zowona - Mulungu adabwera pa dziko lapansi. Izi ndi zodabwitsa!

Kuti akhale Mpulumutsi Yahweh adasandulika munthu. Izitu sizikutanthawuza kuti Iye adaleka kukhala Mulungu. Komabe, Ambuye adadziwa kuti njira yokhayo yakutipulumutsira idali yakuti Iyeyo akhale monga ife anthu. Chifukwa cha chimenechi Iye adalowa m'dziko lapansi ngati khanda, monga momwe khanda lililonse limafikira m'dziko lapansi.

Yahweh adabadwa m'banja monga banja lina lililonse. Dzina la amayi wake lidali Mariya ndipo mwamuna wake wa mayiyu adali Yosefe. Ngakhale banja limeneli lidali monga banja lina lililonse, khandali silidali la choncho. Iye adali woyera - wosiyana ndi wina aliyense!

Khandali lidali Mulungu Mwini.


Yahweh sadabadwire m'chipatala. Iye adabadwira m'khola - malo amene mumakhala nkhosa komanso ana a nkhosa.

Alendo ake oyambirira adali abusa - anthu woweta ndi kusamalira nkhosa.

Mulungu atabwera ku dziko lapansi, dzina lake lidali Yesu. Dzina lakuti Yesu limatathawuza kuti 'Yahweh ndiye amapulumsa.'

Yesu ndiye Mpulumutsi uja amene Mulungu adalonjeza Adamu ndi Hava zaka zambirimbi zapitazo. Iye adabwera kuti adzatipulumutse ife ku chilango choyenera tchimo lathu


Khisimisi ndi Mbiri yofotokozera kuti Yahweh adabwera pa dziko lapansi monga khanda. Nyengo ya Khisimisi timapatsana mphatso ndi cholinga chokumbutsana kuti Mulungu adatipatsa mphatso yayikulu kwambiri. Mphatso imene Mulungu adatipatsa ndi Mpulumutsi. Ifetu timakondwera pa Nyengo ya Khisimisi, chifukwa Khisimisi imatikumbutsa kuti Mulungu amasunga malonjezano ake.




Pamene Yesu adakula msinkhu adayamba kuchita zinthu zodabwitsa. Adapenyetsa akhungu komaso adachiritsa anthu amene sankatha kuyenda. Iyeyu adachiritsa anthu ambiri wodwala – enanso wodwala matenda owopsa monga khate. Yesu adalinso ndi mphamvu ngakhale pa imfa. Iye adapangitsa kuti anthu amene adafa akhalenso ndi moyo.

Nthawi ina yake, Iye adadyetsa gulu lalikulu la anthu amene adali ndi njala. Padalitu mazanamazana a anthu koma Yesu adali ndi mikate isanu yokha ndi nsomba ziwiri. Komabe, pamene anthu ankamuthandiza Yesu kugawa chakudya, mkate uja ndiponso nsomba zimachulukirachulukira! Munthu aliyense adalandira chakudya chomukwanira. Atamaliza, adatolera madengu khumi ndi awiri a zakudya zotsala.

Anthu onse adawona kuti Yesu amakonda anthu. Yesu adachita zonsezi kuti aliyense adziwe kuti Iye adali Mulungu.






Usiku wina wake, ena mwa anzake a Yesu adaganiza kuti awoloke nyanja pa bwato. Pamene iwo adafika pakati pa madzi, adakumana ndi namondwe owopsa. Kudali mphepo yochititsa mantha ndipo mafunde akulu adawomba bwato lija.

Usiku onse anthu aja adayesa kupalasira bwato ku mtunda, koma mphepo ija idali ya mphamvu kwambiri. Nthawi ya kum'bandakucha, anthu aja adawona Munthu ali kuyenda pakati pa madzi. Iwo adaganiza kuti adali mzungu! Iwowa adachita mantha.

Ndipo kenaka adamva mawu akuyankhula kwa iwo ndi kuti, 'Ndine amene, musachite mantha.' Uyutu adali Yesu!

Ndipo Peturo adayankhula mokweza mawu ali m'bwato muja, 'Ambuye! Ngati ndi Inuyo, mundilore ndibwere kwa inu pa madzipa'.

Yesu adati, 'Tabwera kuno'.



Peturo adatuluka m'bwato. Iye adayamba kuyenda pamwamba pa madzi ndi kumapita kumene kudali Yesu.

Komabe, pamene Peturo adawona mphepo ndiponso mafunde, iye adachita mantha ndipo adayamba kumira. Kodi iyeyu adayenera kuchita chiyani?

Iyeyu akadakhoza kuyesetsa mwa iye yekha, kapena akadampempha Yesu kuti amupulumutse. Kodi iyeyu adayenera kudalira ndani?

Peturo adazindikira kuti sakadakhoza kudzipulumutsa yekha - ndi Yesu yekha amene akadamupulumutsa iye. Tsono iye adafuwula, 'Ambuye mundipulumutse ine!' Ndipo Yesu adatambasula dzanja lake ndi kumugwira Peturo. Peturo adapanga chisankho chabwino.

Monga momwe Peturo sakadathera kudzipulumutsa yekha pa madzi paja, ifenso sitingathe kudzipulumutsa ku chilango cha uchimo. Ife tikusoweka Mpulumutsi.

Baibulo limanena kuti Yesu ndiye Mpulumutsi wathu. Tiyenera kumudalira Iye.



Pamene adali pa dziko lapansi, Yesu adakhala monga momwe munthu wina aliyense amakhaira. Iye adagwira ntchito yopala matabwa komanso amakacheza kwa anzake. Iyeyu ankadya, ankagona ndiponso ankapita ku malo wosiyanasiyana. Komabe, Yesu adalinsu wosiyana ndi inu ndi ine. Yesu sadachitepo kanthu kalikonse koyipa.

Nthawi yonse imene adakhala pa dziko lapansi, ngakhale ngati kam'nyamata kakang'ono, Iye sadachitepo ngakhale kanthu kamodzi koyipa. Yesu ndi yekhayo amene adakhala moyo wangwiro. Iye adali munthu wosiyana ndi anthu wonse.

Popeza Yesu adakhala moyo wangwiro, Iyeyu adalibe tchimo limene lidayenera kulandira chilango. Iye sadayenera kufa. Anthu amafa chifukwa cha tchimo koma Yesu sadachimweko.

Ngakhale Yesu sadayenera kufa, Iye ankawawuza anthu kuti tsiku lina anthu adzamupha. Iwo adzamumenya Iye, kumukwapula kambirimbiri ndi chikoti. Kenaka iwo adzamukhoma ndi misomali yayikulu m'manja ndiponso ku mapazi ake ndi kumupachika Iye pa mtanda. Ndipo Yesu adzafa. Iye atakhala chikhalire wakufa masiku atatu, adzawuka nadzakhalanso ndi moyo.



Anthu amene adamumva Iye akunena zimenezi sadamukhulupirire. Iwo adamuwuza kuti Iye asamayankhula zinthu zotero, koma zimene Yesu ankanena zidali zowona. Iye adawawuza anzakewo zonse zimene Mulungu adakonza - Iyeyu adawawuza Uthenga Wabwino.

Udali Uthenga wokhudza malonjezano a Mulungu - udali Uthenga wa Mwanawankhosa.

Kodi mukumukumbukira Mwanawankhosa uja?

Dzina lina la Yesu lidali Mwanawankhosa wa Mulungu.

Kodi mukukumbukira kuti Mwanawankhosayu ankayenera kukhala wa mwamuna?

Inde, Yesu adali munthu wa mwamuna.

Mwanawankhosa ankayeneranso kukhala wangwiro.

Yesu adali wangwiro - Iye adalibe tchimo.



Mulungu adawuza munthu kuti ankayenera kubweretsa mwanawankhosa ku guwa la nsembe, malo a paderadera a imfa.

Pamene adali pa dziko lapansi, Yesu adalola kuti anthu amutengere ku mtanda, malo a paderadera a imfa.

Kodi mukukumbukira m'mene munthu amene wabweretsa mwanawankhosa amayikira dzanja lake pa mutu pa mwanawankhosayo? Izi zinkasonyeza kuti munthuyo wayika tchimo lake pa mwanawankhosa.

Baibulo limanena kuti pamene Yesu adali pa mtanda, Iye adasenza machimo athu kwa Iye yekha. Iye adatenga machimo a anthu onse kuyambira anthu abwino kwambiri kufikira abambo ndi amayi amene ali oyipitsitsa.

Yesu adamva mawu onse wonyoza amene anthu ankayankhula. Iye adadziwa zinthu zoyipa zonse zimene anthu adazichita. Iye adawona mkwiyo onse umene anthu adawonetsa. Iye adamva ululu onse umene anthu adayambitsa. Yesu wangwiroyo adadzitengera pa Iye yekha zotsatira zonse za zoyipa za machimo athu. Iyeyu adamva zonsezi, Iye adazidziwa zonse ndipo adazitenga zonse. Ziyenera kuti zidali zinthu zowopsa.

Inde, Uthenga wonsewu umanena za mwanawankhosa.

Yesu adali Mwanawankhosa - Mwanawankhosa wathu.

Tsopano takumbukirani nkhani yonse. Kodi mukukumbukira zimene zinkachitika ndi mwanawankhosa? Popeza Mulungu ayenera kulanga tchimo, ndipo kuti chilango chake ndi imfa, mwanawankhosa ankayenera kufa.


Izi zidali chomwecho ndi Yesu.

Popeza Yesu adatenga machimo athu onse, Iye adayenera kulandira chilango. Yesu adayenera kufa.

Baibulo limanena kuti Yesu adafa m'malo mwathu. Iye adalandira chilango chonse chimene chidayenera machimo athu, kuti ife tisadzalawe Imfa ya Chiwiri.

Yesu adali Mwanawankhosa wotsiriza - munthu sadayenera kuperekanso nsembe ya mwanawankhosa pa guwa la nsembe. Yesu adakwaniritsa zonse.

Ambuye Yahweh adasunga lonjezano lake.



Nkhaniyi ikadatha Yesu akadali wakufa pa mtanda, ikadakhala yomvetsa chisoni.


Komabe Baibulo limatiwuzanso zambiri. Limatiwuzwa kuti Yesu atafa, abwenzi ake adachotsa thupi lake pa mtanda. Iwo adakamuyika Iye ku manda a paderadera. Manda amenewa adali ngati phanga - kachipinda kakang'ono kopangidwa mong'amba thanthwe lolimba. Pang'onopang'ono, iwo adakankha mwala wawukulu ndi kutseka khomo la mandawo. Kenaka, iwo adabwerera ku mudzi ndi chisoni.

Tsiku lotsatira, anthu aja adapha Yesu adalamulira asilikali kuti alondele manda aja. Iwo adadziwa kuti Yesu ankawawuzwa anthu kuti akadzafa adzawuka patapita masiku atatu. Iwowa sadafune konse kuti wina abe thupi la Yesu ndi kunamizira kuti Iye alinso ndi moyo. Iwo adafunitsitsa kuti thupi lake likhalebe lakufa m'manda muja.

Ngakhale izi zidali choncho, asilikali ngakhale mwala wawukulu sizikadakhocha kulepheretsa Mulungu. Palibe chimene chikadakhocha kulepheretsa ndondomeko ya Mulungu. Monga Yesu adanena kale, patapita masiku atatu, Iye adawuka kwa akufa! Yesu adali ndi moyo.

M'ngelo adagudubuza mwala ndi kuwuchotsa pakhomo kuti aliyense awone kuti m'manda mudalibe Yesu. Atawona m'ngeloyo, alonda aja adachita mantha ndi kunjenjera ndipo adakhala ngati anthu akufa.

Kenaka, pamene azimayi ena adapita ku manda, alonda onse adali atathawa. M'ngelo yekha adakhallira komweko kuti awafotokozere chimene chidachitika. Azimayi amenewa adali anthu woyamba kuwona Yesu wa moyo atawuka kwa akufa.



Kwa masiku makumi anayi, Yesu adawonekera kwa abwenzi ake ndi magulu akulu a anthu. Aliyense adali okondwera. Iye adali kuyankhula, kudya, komanso kuyendayenda ndi iwo. Izi zidali zodabwitsa!

Yesu adali ndi moyo!

Anthu sadakhulupirire izi. Padalibe wina amene adachita zotere m'mbuyomu. Padalibe wina amene atafa adadzidzutsanso kwa akufa!

Yesu adawawonetsera kuti popeza Iyeyo ndi Mulungu, adali wamphamvu zoposa imfa. Anthu sadayeneranso kuwopa kuti adzafa ndiponso kupita ku Nyanja ya Moto. Iwo sadayenera kuchita mantha ndi Imfa ya Chiwiri. Yesu adali ndi mphamvu zokwanira kuwabwezeranso ku moyo.

Komabe, Iye sadzawabwezeranso kuti adzakhaleenso ndi moyo pa dziko lapansi pano - malo amene adawonongedwa ndi tchimo. M'malo mwake, Iye adzawatengera Kumwamba - malo angwiro komanso wodzala ndi chimwemwe.



Yesu ankalonjeza kuti adzachita izi kwa anthu onse amene adzamudalira Iye. Zidalitu zosavuta chonchi.

Anthu onse adayenera kungokhulupirira kuti Yesu adali Mwanawankhosa wawo - kuti Iye adalandira chilango m'malo mwa machimo awo. Iwo adayenera kudalira Yesu ndi kukhulupira kuti Iye adali owona. Kenaka, atakhala moyo wawo padziko lapansi pano, Yesu adzawasandutsa angwiro kuti akakhale Kumwamba.


Izi zidali zowona kwa anthu wochokera m'mayiko onse kaya ndi amuna, akazi, anyamata kapenanso atsikana. Aliyense amene adzadalira Yesu adzakhala ndi moyo nthawi zonse Kumwamba.

Anthu adamvetsera mokondwera. Iyi idali nkhani imene aliyense adafuna kuyimva. Iwowa adakambirana ndi Yesu kwa mawola angapo zokhudzana ndi ndondomeko imeneyi. Kenaka, patapita masiku makumi anayi, Yesu adawatsanzika kubwerera kwawo Kumwamba. Iye amakhala kumeneko kufikira tsopano, kwawo ku dziko langwiro.

Izitu ndi zimene Nyengo ya Pasaka imafotokoza. Nyengo imeneyi, ife timaganizira za imfa ya Yesu ya pa mtanda. Timakumbukira m'mene abwenzi ake a Yesu adamuyikira m'manda komanso m'mene adawukitsidwira kwa akufa. Ndi nthawi ya paderadera imene timakumbukira kuti Yahweh adabwera pa dziko lapansi. Nyengo ya Pasaka, timamva chisoni kuti Yesu adafa, komanso timayamika chifukwa Iye sadakhale chikhali wakufa. Timakhala wokondwera chifukwa Iye ndi wamoyo.

Inde! Baibulo lonse ndi mbiri ya tanthawuzo la Khisimisi ndi Nyengo ya Pasaka.

Iyi ndi kalata yochokera kwa Mulungu –yodzala ndi chikondi. Imafotokoza za Mwanawankhosa wathu.



Kodi kalata ya Mulunguyi mumayimvetsetsa?

Onani mayankho pa tsamba 54

Kalata ya Yahweh – Buku Lopatulika – ndiyofunika kwambiri ndipo muyenera kuyesetsa kuti muyizindikire bwinobwino. Kwa kanthawi tayankhani mafunso wotsatirawa. Mafunso amenewa adzakuthandizani kudziwa mmene mumamvetsetsera ndondomeko ya Mulungu. Ngati mupereke mayankho wolakwika a ena mwa mafunso amenewa, muyenera kuwerenganso buku lino kufikira mayankho wonse mutawazindikira.

1. Mulungu adalenga zinthu zonse ndi mawu wokha. Kodi zimenezi zimatiwuzza zotani za Yahweh?
2. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu adali nako kuthekera kolenga dziko langwiro lokha?
3. Baibulo limagwiritsa ntchito liwu limodzi pofuna kufotokozera chisankho chimene Lusifala adapanga pofuna kusamvera Mulungu. Kodi ndi liwu lanji limeneli?
4. Kodi ndi chifukwa chiyani chili chinthu cholakwika kuti munthu akachita chinthu choyipa asamalandira chilango?
5. Kodi malo amene Yahweh adalengera Satana ndi angelo woyipa amatchedwa chiyani?
6. Baibulo limagwiritsa ntchito liwu lina lake pofuna kufotokoza chisankho chosamvera Mulungu chimene Adamu ndi Hava adapanga. Kodi liwu limeneli ndi liwu lanji?
7. Kodi ndi chiyani chimene chidabwera m'dziko lapansi ngati chotsatira cha wuchimo?
8. Chifukwa cha tchimo lawo, Adamu ndi Hava sadali angwiro. Choncho, pamene adafa adayenera kukakhala ndi Satana m'Nyanja ya Moto. Kodi imfa yotereyi Baibulo limayittha chiyani?
9. Mulungu adalonjeza kuti adzatumiza munthu wapaderadera kuti adzapulumutse anthu wonse ku Imfa ya Chiwiri. Kodi Baibulo limamuttha ndani munthu ameneyu?
10. Ndi chifukwa chiyani Mulungu amayenera kuwapanga anthu kuti akhale angwiro kuti akakhale ndi Iye Kumwamba?

11. Kodi zikadatheka kuti Mulungu angophiphiritsa kuti tchimo la Adamu ndi Hava likhale ngati silidachitike?
12. Mulungu adawawonetsera anthu mmene Iye akadaperekera chilango ku tchimo koma wosawalanga anthuwo. Kodi ndi nyama yanji yimene Mulungu adawawuzza anthuwo kuti azibweretsa?
13. Kodi chimachitika ndi chiyani ndi tchimo la munthu munthuyo akasanjika dzanja lake pa mutu wa mwanawankhosa?
14. Kodi mwanawankhosa adafera yani?
15. Popeza mwanawankhosa sadachite choyipa chilichonse, ndi chifukwa chiyani adayenera kulandira chilango?
16. Ngati anthu akhulupirira Yahweh, akamwalira adzapita Kumwamba. Kodi Mulungu amawasinthwa bwanji anthuwa kuti akakhale ndi Iye mdziko lake langwiro?
17. Kodi titamachita zinthu zabwino moyo wathu wonse, ntchito zabwinozi zikhoza kutipangitsa kuti tikalowe Kumwamba?
18. Kodi ndani amene adachokera Kumwamba ndi kudzakhala Mpulumutsi wa dziko lapansi?
19. Popeza Yesu adalibe tchimo, kodi adayenera kufa?
20. Baibulo limanena kuti Yesu adali ngati ana wa nkhosawa amene anthu ankadzapereka pa guwa lansembe. Kodi ndi dzina lanji limene Baibulo limapereka kwa Yesu pofuna kutikumbutsa ife za ana wa nkhosawa?
21. Baibulo limanena kuti mwanawankhosa adatenga wuchimo wa anthu wonse. Kodi ndi tchimo la ndani limene Yesu adatenga pa Iye yekha?
22. Mwanawankhosa adafa mmalo mwa anthu. Kodi Yesu adafera yani?
23. Kodi anthu ayenera azichita chiyani kuti Yesu awatenge kukakhala naye Kumwamba?

Zimene mwawerenga m'buku lino ndi gawo laling'ono chabe la zimene Buku Lopatulika limanena za ndondomeko ya Mulungu. Baibulo limafotokoza nkhani zambirimbiri za momwe Mulungu akhoza kutilandirira. Ngati mukufuna kudziwa zambiri, onani tsamba 66.

Kodi inu mumakhulupirira kalata ya Mulungu?

Onani mayankho pa tsamba 54

Ngati mwayankha mafunso wonse mokhoza, ndiye kuti mumamvetsetsa ndondomeko zake za Mulungu. Kungomvetsetsa kalata ya Mulungu ndi chinthu chabwino kwambiri, komabe, ndizosakwanira. Muyenera kupanga chiganizo. Kodi mukuwona inu, ndi chinthu china kumvetsetsa Baibulo, koma ndi chinthu chinanso kulikhulupirira.

Tayesani kuyankha mafunso awa. Mafunso amenewa adzakuthandizani kuti mudziwe ngati mumakhulupirira kalata ya Mulungu.

1. Kodi Yahweh atabwera padziko lapansi, adasiya kukhala Mulungu?
2. Kodi Yesu ndani? Kodi mumakhulupirira kuti Yesu ndi Yahweh?
3. Mulungu ndi wangwiro. Kodi inu ndinu wangwiro? Kodi inuyo mumakhulupirira kuti ndinu wabwino ndiponso woyenera kukhala Kumwamba, kapena mumakhulupirira kuti ndinu wochimwa?
4. Kodi inuyo mumakhulupirira kuti Mulungu adzalanga tchimo lonse?
5. Kodi ndani amene adatenga chilango cha wuchimo wanu?
6. Kodi inuyo mumakhulupirira kuti Yesu ndiye Mwanawankhosa wanu?
7. Yesu atafa, Iye adawuka kwa akufa ndipo amakhala Kumwamba. Kodi inuyo mumakhulupirira kuti zimenezi ndi zowona?

Kodi munapereka mayankho wokhoza a mafunso amenewa? Kodi inuyo mukukhulupirira kuti mayankho anu ndi owona? Ngati zili choncho, dziwani kuti Baibulo likunena kuti Yesu adalandira chilango mmalo mwa inu. Iyeyu ndiye Mpulumutsi wanu. Inu simudzachitanso mantha ndi Imfa ya Chiwiri.

Inu mukakhulupirira kuti Baibulo limanena zowona, ndiye kuti mumamudalira Yahweh. Popeza mumamudalira Iye, Mulungu

akuti ndinu bwenzi lake. Iye amalonjeza kuti sadzakusiyani. Iye adzakhala ndi inu nthawi zonse, ngakhale mutakhala kuti mwakakhala malo a mtundu wanji kapena mwachita zotani.

Pamene inu mwatsiriza kukhala padziko lapansi pano, Mulungu akuti adzakusandutsani wangwiro ndi woyenera kukhala Kumwamba. Inu mudzakhala ndi Iye nthawi zonse. Uwu ndi uthenga wabwino! Ichi ndi chinthu chimene mukhoza kuchidziwa motsimikizika mtima chifukwa Mulungu ndi amene akunena zimenezi ndipo Mulungu samanena bodza.

Kapena mwina buku lino lakuyankhani mafunso ambiri amene munali nawo. Baibulo ndilodzala ndi nkhani za mtundu wumenewu. M'menemu mumapezeka mayankho a moyo wumene mumayenera kukhala tsiku ndi tsiku. Zikhoza kukhala bwino kutenga Baibulo ndi kuyamba kuwerenga chigawo chimene chimatchedwa 'Uthenga Wabwino wa Yohane'. Patulani nthawi yakuti muziwerenga Baibulo tsiku ndi tsiku.

Pali chinthu chimodzi chotsiriza chimene ndi chofunikira kuchitchula. Munthu wina akakuchitirani chinthu chapaderadera, mumamuthokoza. Baibulo limanena kuti inu mukhoza kuyankhula kwa Ambuye monga mmene munthu amayankhulira kwa bwenzi lake. Baibulo limatcha kuyankhula kotere kuti ndi pemphero.

Awa ndi ena mwa mawu amene munganene pofuna kunena kuti 'zikomo' kwa Yesu chifukwa cha zinthu zimene Iye adakuchitirani. Mukhoza kupemphera ndi kumuthokoza Iye pogwiritsa ntchito mawu anu. Muyenera kukumbukira kuti Mulungu ali poseponse – Iye akumvetsera.

Ambuye Yesu, ine ndidziwa kuti Inu ndinu Mulungu ndipo mudalenga zinthu zonse. Inu ndinu wangwiro; koma ine ndine wochimwa. Ndinu nokha amene mukhoza kundipulumutsa ine. Ndikhulupirira kuti mudafa imfa ya pamtanda ndikulandira chilango chifukwa cha machimo anga. Ine ndikhulupirira kuti Inu ndinu Mpulumutsi wanga. Zikomo chifukwa chachikondi chanu chachikulu pa ine. Ndidziwa kuti mudzasunga lonjezano lanu lakunditenga ine kupita kwanu Kumwamba kumene ndikakhale ndi Inu.

Indedi, Yesu ndiye Mpulumutsi wodabwitsa.

Mayankho

1. Ndi wamphamvu. (tsamba 4 mpaka 8)
2. Ndi wangwiro. (tsamba 10)
3. Tchimo (Tsamba 10)
4. Sichilungamo (kapena sibwino). Choyipa chilichonse chiyenera kulangidwa. (tsamba 10)
5. Nyanja ya Moto (tsamba 12)
6. Tchimo (tsamba 18)
7. Imfa (tsamba 18)
8. Imfa ya Chiwiri (tsamba 20)
9. Mpulumutsi (tsamba 20)
10. Ndi anthu angwiro wokha amene akhoza kukhala ndi Mulungu wangwiro. (tsamba 24)
11. Iyayi (tsamba 24)
12. Mwanawankhosa (tsamba 24)
13. Mwanawankhosa adachotsa tchimo la anthu. (tsamba 26)
14. M'malo mwa munthu (tsamba 26)
15. Adatenga tchimo la anthu (tsamba 26)
16. Amawapanga iwo kuti akhale angwiro (tsamba 27)
17. Iyayi (tsamba 31)
18. Mulungu, Yahweh, Yesu (ndi chimodzimidzi) (tsamba 32)
19. Iyayi (tsamba 40)
20. Baibulo limamutcha Yesu "Mwanawankhosa wa Mulungu" (tsamba 41)
21. Tchimo lathu (tsamba 42)
22. M'malo mwathu (tsamba 43)
23. Dalirani Iye kapena khulupirirani Iye (tsamba 48)

Mayankho

1. Iyayi, Iye sadasiye kukhala Mulungu.
2. Yesu ndi Mulungu, Yesu ndi Yahweh.
3. Ndine wochimwa.
4. Inde
5. Mulungu, Yesu
6. Inde
7. Inde, ndikhulupirira kuti ndi zoon.

Ndime za m'Baibulo

Mawu alimmuniwa ndi wochokera m'Baibulo. Mukhoza kuwapeza mu ndime zimene zalembedwa kutsogolo kwa mawuwo.

Tsamba 2 ndi 3

Yesaya 45:5 Ine ndili Yehova ... ndipo Palibe winanso, popanda Ine palibe Mulungu.

Yeremiya 10:6 Chifukwa palibe akunga Inu, Yehova. Muli wamkulu ndipo dzina lanu lili lalikulu ndi lamphamvu.

Yesaya 40:26,28 Kwezani maso anu Kumwamba! Muwone amene analenga izo ... amene atulutsa khamu lawo ndi kuziwerenga. Popeza ali wolimba mphamvu, palibe yimodzi yisoweka ... Mulungu wachikhalire, Yehova, Mlengi wa malekezera a dziko lapansi, salefuka konse, salema. Nzeru zake sizisanthulika.

Masalmo 145:3 Yehova ndi wamkulu ... ndi ukulu wake ndi wosanthulika!
Yohane 4:24 Mulungu ndi Mzimu.

Ahebri 1:14 Kodi siyili yonse mizimu yotumikira`

Masalmo 103:20,21 Lemekezani Yehova, inu angelo ake. Amphamvu zolimba. Akuchita Mawu ake. Inu atumiki ake akuchita chomkondweretsa lye.

Tsamba 4 ndi 5

Ahebri 11:3 Ndi chikhulupiriro tizindikira kuti mayiko ndi a m'mwamba womwe adakonzedwa ndi mawu a Mulungu, kotero kuti zinthu zopenyeka sizidapangidwa zochokera mwa zinthu zowonekazo.

Genesis 1:3 Ndipo anati Mulungu, 'Kuyere.' Ndipo kunayera.

Yeremiya 32:17 Ha! Yehova Mulungu, tawonani, Inu munalenga Kumwamba ndi dziko lapansi ndi mphamvu yanu yaikuru ndi mkono wanu wotambasuka; palibe chokulakani Inu.

Genesis 1:16 Ndipo Mulungu anapanga zowunikira zazikulu wiwiri; chowunikira chachikulu chakulamulira usana chowunikira chaching'ono chakulamulira usiku, ndi nyenyezi zomwe.

Yeremiya 23:24 'Kodi munthu angathe kubisala mobisika kuti ndisamuwone iye?' ati Yehova.

Genesis 1:1 Pachiyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi.

Eksodo 20:11 Chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamaliza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse zili m'menemo.

Genesis 1:21 ...adalenga zinsomba zazikulu ndi zoyendayenda zamoyo zakuchuluka m'madzi mwa mitundu yawo, ndi mbalame zamapiko.

Genesis 1:25 Ndipo Mulungu adapanga zinyama za dziko lapansi monga mwa mitundu yawo; ndi ng'ombe monga mwa mtundu wake, ndi zonse zakukwawa pansu monga mwa mitundu yawo.

Genesis 2:7 Ndipo Yehova anaumba munthu ndi dothi lapansi.

Tsamba 6 ndi 7

Yesaya 44:24 Atero Yehova, Mombolo wako, 'ndi Iye amene anakuumba iwe m'mimba, Ine ndine Yehova, amene ndipanga zinthu zonse, ndi kufunyulula ndekha zakumwamba, ndi kuyala dziko lapansi; ndani ali ndi Ine?'

Masalmo 24:1 Dziko lapansi nlaYehova ndi zodzala zake zomwe, dziko lokhalamo anthu ndi iwo wokhala m'mwemo.

1 Timoteo 6:17 ...Mulungu amene atipatsa ife zonse kochulukira, kuti tikondwere nazo.

Genesis 1:31 Ndipo anaziwona Mulungu zonse zimene adazipanga, ndipo tawonani, zinali zabwino ndithu.

Tsamba 8 ndi 9

Deuteronomo 32:4 Thanthwe, ntchito yake ndi yangwiwo; Pakuti njira zake zonse ndi chiweruzo; Mulungu wokhulupirika ndi wopanda chisalungamo; Iye ndiye Wolungama ndi Wolunjika.

Masalmo 89:14 Chilungamo ndi chiweruzo ndiwo maziko a mpando wachifumu wanu; chifundo ndi choonadi zitsogolera pankhope panu.

Chibvumbulutso 21:27 Ndipo simudzalowa konse momwemo kanthu kali konse kosapatulidwa kapena iye wakuchita chonyansa ndi bodza; koma iwo wokha wolembedwa m'buku la moyo la Mwanawankhosa.

Chibvumbulutso 21:3 Ndipo adzakhalitsa nawo, Ndi iwo adzakhalala anthu ake, ndi Mulungu yekha adzakhalala nawo, Mulungu wawo.

Chibvumbulutso 21:10 - 12, 25 ... Ndipo unakhala nawo ulemerero wa Mulungu; kuunika kwake kunafanana ndi mwala wa mtengo wake woposa ... nukhala nalo linga lalikulu ndi lalitali ... Ndipo pa zipata pake sipatsekedwa konse usana, pakuti sikudzakala usiku komweko.

Chibvumbulutso 21:21 Ndipo khwalala la mzinda nlagolidi woyengeka, ngati mandala openyekera.

Chibvumbulutso 22:1 Ndipo anandionetsa mtsinje wa madzi a moyo, wonyezimira ngati krustalo.

Chibvumbulutso 22:5 Ndipo sikudzakhalanso usiku; ndipo sasowa kuunika kwa nyali, ndi kuunika kwa dzuwa; chifukwa Ambuye Mulungu adzawaunikira.

Chibvumbulutso 21:4 Ndipo adzawapukutira misozi yonse kuichotsa pa maso pao; ndipo sipadzakhalanso imfa; ndipo sipadzakhalanso maliro kapena kulira kapena chowawitsa.

Chibvumbulutso 21:5 Ndipo Iye wakukhala pa mpando wachifumu anati, 'Taonani, ndichita zonse zikhale zatsopano.'

Tsamba 10 ndi 11

1 Yohane 3:4 Yense wakuchita tchimo achitanso kusayeruzika, ndipo tchimo ndilo kusayeruzika.

Yesaya 14:12-14 Wagwadi kuchokera Kumwamba. Iwe nthanda, mwana wa m'bandakucha! ... Ndipo iwe unati mumtima mwako, "... ndidza ... ndidzafanana ndi Wammwambamwamba."

Miyambo 6:16-17 Zilipo zinthu zisanu ndi chimodzi Mulungu azida; ngakhale zisanu ndi ziwiri zimnyansa; maso akunyada, lilime lonama, Ndi manja akupha anthu osachimwa;

Mlaliki 12:14 Pakuti Mulungui adzanena mlandu wa zochita zonse, ndi zobisika zonse, ngakhale zabwino ngakhale zoipa.

Tsamba 12 ndi 13

Ezekiel 28:16-17 ... chifukwa chake ndinakukankha kukuchotsa pa phiri la Mulungu; ndipo ndinakuwononga Kerubi wakuphimba iwe, kukuchotsa pakati pa miyala ya moto. ... Unadzikuza mtima chifukwa cha kukongola kwako, waipsa nzeru zako; chifukwa cha kuwala kwako ndakugwetsa pansu. **Chibvumbulutso 20:10** Ndipo mdiereklezi wakusokeretsa anaponyedwa mnyanja ya moto ndi sulfure, ... ndipo adzakuzunza usana ndi usiku ku nthawi za nthawi.

Mateyu 25:41 Chokani kwa Ine wotembereredwa inu ku moto wa nthawi zonse wokolezedwera mdierেকেzi ndi a mithenga ake.

Tsamba 14 ndi 15

Genesis 1:27 Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chake, m'chifanizo cha Mulungu adalenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi.

Genesis 2:15 Ndipo Yehova Mulungu anatenga munthuyo, namuika iye m'munda wa Edene.

Genesis 2:9 Ndipo Yehova Mulungu anameretsa m'nthaka mitengo yonse yokoma m'maso ndi yabwino kudya; ndiponso mtengo wa moyo pakati pa mundapo, ndi mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa.

Genesis 2:16-17 Ndipo Yehova Mulungu anamuza munthuyo nati, 'Mitengo yonse ya m'munda udyeko; ... koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa usadye umenewo; chifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu.

Tsamba 16 ndi 17

Genesis 3:1, 4-5 ... Ndipo njoka (amene ali Satana) inati kwa mkaziyo, 'Ea! Kodi anatitu Mulungu, Usadye mitengo yonse ya m'mundamu? ... Njokayo ndipo inati kwa mkaziyo, 'Kufa simudzafai; chifukwa adziwa Mulungu kuti tsiku limene mukadya umenewo, adzatseguka maso anu, ndipo mudzakhalala ngati Mulungu, wakudziwa zabwino ndi zoipa.'

Tsamba 18 ndi 19

Genesis 3:6 Ndipo pamene anawona mkaziyo kuti mtengo unali wabwino kudya, ... wakupatsa nzeru, anatenga zipatso zake, nadya, napatsanso mwamuna wake amene ali naye, nadya iyenso.

Genesis 3:19 M'thukuta la nkhope yako udzadya chakudya, kufikira kuti udzabwerera kunkhaka, chifukwa kuti m'menemo unatengedwa; chifukwa kuti ndiwe fumbi, ndi kufumbiko udzabwerera.

Aroma 8:22 Pakuti tidziwa kuti cholengedwa chonse chibuwula, ndi kugwidwa m'zowawa pamodzi kufikira tsopano.

Aroma 5:12 Chifukwa chake monga uchimo udalowa m'dziko lapansi mwa munthu m'modzi, ndi imfa mwa uchimo; chotero imfa idafikira anthu onse; chifukwa kuti onse adachimwa.

Rom 6:23 Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi Imfa.

Yesaya 59:2 Koma zoyipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu; ndipo machismo anu abisa nkhope yake kwa inu.

Akolose 1:21 Ndipo inu, wokhala alendo akale ndi adani m'chifuwa chanu m'ntchito zoyipazo.

Tsamba 20 ndi 21

Chibvumbulutsa 21:8 Koma amantha, ndi wosakhulupirika, ndi wonyansa, ndi ambanda, ndi achigololo, ndi anyanga ndi wolambira mafano, ndi onse abodza, cholandira chawo chidzakhala m'nyanja yotentha ndi moto ndi Sulfure; ndiyo imfa yachiwiri.

Yesaya 54:8 ... koma ndi kukoma mtima kwa chikhalire ndidzakuchitira chifundo, ati Yehova mombolo wako.

Yesaya 43:11 Ine, Inetu ndine Yehova; ndipo palibe mpulumutsi, koma Ine ndekha.

Tsamba 22 ndi 23

Ahebri 11:1 Tsopano chikhulupiriro ndicho chikhazikitso cha zinthu zoyembekezeka, chiyesero cha zinthu zosapenyeka.

Ahebri 11:6 Koma wopanda chikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa lye.

Masalmo 27:1 Yehova ndiye kuunika kwanga ndi chipulumutso change; ndidzaopa yani? Yehova ndiye mphamvu ya moyo wanga; ndidzachita mantha ndi yani?

Masalmo 118:8, 14 Kuthawira kwa Yehova nkokoma koposa kukhulupirira munthu ...

Masalmo 115:11 Inu akuopa Yehova, ... khulupirirani Yehova.

Tsamba 24 ndi 25

Arom 3:23 Pakuti onse adachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu.

2 Samuel 14:14 Pakuti kufa tidzafa, ndipo tili ngati madzi otayika pansu amene sakhoza kuwawolanso; ngakhale Mulungu sachotsa moyo, koma alingalira njira yakuti wotaikayo asakhale womtayikira lye.

Levitiko 5:17-18 Ndipo munthu akachimwa, nachita china cha zinthu zilizonse aziletsa Yehova; angakhale analibe kudziwa, koma wapalamula, azisenza mphulupulu zake. Nadze nayo kwa wa nsembe nkhoa ya mphongo wopanda chilema ya mkhola lake.

Levitiko 1:4 Ndipo aike dzanja lake pa mutu pa nsembe yopsereza; ndipo idzalandidiridwa mmalo mwake, imtetezere.

Levitiko 5:17-18 Ndipo adzakhululukidwa.

Tsamba 26 ndi 27

Miyambo 3:5 Khulupirira Yehova ndi mtima wako onse. Osachirikizika pa luntha lako!

Tsamba 28 ndi 29

Eksodo 20:23 Musapange milungu yasiliva ikhale pamodzi ndi Ine, musadzipangire milungu ya golidi.

Eksodo 20:2-5 ... Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena chifaniziro chili chonse cha zinthu za thambo la kumwamba, kapena za m'madzi a pansu pa dziko; usazipembedzere izo.

1Akorinto 10:20 - 21 Simungathe kumwera chikho cha Ambuye, ndi chikho cha ziwanda; simungathe kulandirako ku gome la Ambuye ndi ku gome la ziwanda.

2 Akorinto 11:14 Pakuti satana yemwe adziwonetsa ngati m'ngelo wa kuwunika.

Aroma 1:24 - Amene adasandutsa chowonadi cha Mulungu chabodza napembedza, natumikira cholengedwa, ndi kusiya Wolengayo, ndiye wodalitsika nthawi yosatha.

Yakobo 2:10 Pakuti aliyense amene asunga malamulo onse, koma akakhumudwa pa limodzi, iyeyu wachimwira onse.

Aroma 3:20 Chifukwa chake pamaso pake palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo; pakuti uchimo udziwika ndi lamulo.

Ahebri 4:12 - Ndipo palibe cholengedwa chosawonekera pamaso pake, koma zonse zikhala pambalambanda ndi zobvundukuka pamaso pake pa lye amene tichita naye.

Tsamba 30 ndi 31

Eksodo 20:12-16 Uzilemekeza atate wako ndi amako; kuti achuluke masiku ako m'dziko limene Yehova Mulungu wako akupatsa iwe. Usaphe. Usachite chigololo. Usabe. Usamnamizire mnzako.

Eksodo 24:12 Ndipo Yehova anati kwa Mose, Ukwere kudza kwa Ine m'phiri muno, nukhale pompano; ndipo ndidzakupatsa magome a miyala, ndi chilamulo ndi malamulo, ndawalemba kuti uwalangize.

Tsamba 32 ndi 33

Masalmo 130:5, 7-8 Ndilindira Yehova, moyo wanga ulindira, ndiyembekeza Mau ake ...

Yesaya 9:6 Pakuti kwa ife Mwana wa khanda wabadwa, kwa ife Mwana wa mwamuna wapatsidwa, ndipo ulaqmuliro udzakhala pa phewa lake, ndipo adzamutcha dzina lake wodabwitsa, wauphungu, Mulungu Wamphamvu, Atate wosatha, Kalonga wa mtendere.

Luka 2:7 Ndipo iye anabala mwana wake wamwamuna woyamba; namukulunga lye mu nsalu, namgoneka modyera ng'ombe, chifukwa kuti adasowa malo m'nyumba ya alendo.

Luka 2:8 - 12 Ndipo padali abusa m'dziko lomwelo, wokhala kubusa ndi kuyang'anira zoweta zawo usiku. Ndipo m'ngelo wa Ambuye adayimilira paiwo, ndi kuwala kwa Ambuye kudawaunikira mozungulira: ndipo adawopa ndi mantha akulu. Ndipo m'ngelo adati kwa iwo, 'Musawope; pakuti onani, ndikuwuzani inu uthenga wabwino wa chikondwerero chachikulu, chimene chidzakhala kwa anthu onse. Pakuti wakubadwirani inu lero, m'mzinda wa Davide, Mpulumutsi, amene ali Khristu Ambuye. Ndipo ichi ndichizindikiro kwa inu: Mudzapeza mwana wakhandu wokutidwa ndi nsalu atagona modyera.'

Mateyu 1:25 ... namutcha dzina lake 'Yesu'.

Tsamba 34 ndi 35

Mat 4:23 - 24 Ndipo Yesu adayendayenda mu Galileya monse, adalikuphunzitsa mu masunagoge mwawo, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumu, nachiritsa kudwala konse ndi nthenda zonse mwa anthu. Ndipo mbiri yake inabuka ku Suriya konse; ndipo adatengera kwa lye onse wodwala, wogwidwa ndi nthenda ndi mazunzo a mitundu mitundu, ... ndipo lye adawachiritsa.

Mateyu 14:13 - 21 Ndipo Yesu adatuluka, nawona khamu lalikulu, ndipo adagwidwa ndi chifundo ndipo anachiritsa wodwala awo. Ndipo pamene panali madzulo, wophunzira ake adafika kwa lye, nanena, 'Malo ano ngachipululu, ndipo nthawi yapita tsopano; kawuzeni khamulo lidzipita ku midzi likadzigulire

lokha kamba'. Koma Yesu adati kwa iwo, 'Iwo alibe chifukwa chopitira, apatseni ndinu adye'. Ndipo iwo adanena kwa lye, 'Ife tiribe kanthu pano koma mikate isanu ndi nsomba ziwiri'. Ndipo lye adati, Mudze nazo kuno kwa Ine. Ndipo lye anadalitsa, nanyema, napatsa mikateyo kwa wophunzira ake ndi wophunzira kwa khamulo. Ndipo adadya onse, nakhuta; ndipo adatola makombo wotsala, mitanga khumi ndi iwiri yodzala. Ndipo adadyawo adali amuna monga zikwi zisanu, kuwaleka akazi ndi ana.

Tsamba 36 ndi 37

Mateyu 14:24 -26, 28-29 Koma chombo tsopano chidafika pakati pa nyanja, chozunzika ndi mafunde; pakuti mphepo idadza mokomana nacho. Ndipo pa ulonda wa chinayi wa usiku, Yesu adadza kwa iwo, akuyenda pamwamba pa nyanja. Ndipo m'mene wophunzirawo adamuwona lye, alikuyenda panyanja, adanthunthumira, nati, 'Ndi mzungu!' Ndipo adafuwula ndi mantha. Ndipo Petro adamyankha lye nati, 'Ambuye, ngati ndinutu, mudiwuzwe ndidze kwa inu pamadzi'. Ndipo lye adati, 'Idza'. Ndipo pamene Petro adatsika m'chombo, nayenda pamwamba pamadzi, kupita kwa Yesu.

Tsamba 38 ndi 39

Mateyu 14:30-31 Koma m'mene iye adawona mphepo yamkuntho, adawopa; ndipo adayamba kumira, nafuwula, nati, 'Ambuye, ndipulumutseni ine!' Ndipo pomwepo Yesu adatansa dzanja lake, namgwira iye, nanena naye, 'Iwe wokhulupirira pang'ono, wakayikiranji mtima?'

Tsamba 40 ndi 41

1Petro 2:22 'Ngakhale sadachita tchimo, ndipo m'kamwa mwake sichidapezedwa chinyengo.'

Ahebri 7:25 - 27 Pakuti mkulu wa ansembe wotere adatiyenera ife, woyera mtima, wopanda choyipa ... Amene alibe chifukwa cha kupereka nsembe tsiku ndi tsiku monga akulu a ansembe, yoyamba chifukwa cha zoyipa za iwo eni, yinayi chifukwa cha zoyipa za anthu; pakuti ichi adachita kamodzi kwatha, podzipereka yekha.

Mateyu 16:21 Kuyambira nthawi imeneyo Yesu adayamba kuwalangiza wophunzira ake, kuti kuyenera lye amuke ku Yerusalemu ndi, kukazunzidwa zambiri ndi akulu, ndi ansembe akulu, ndi alembi; ndi kukaphedwa; ndi tsiku lachitatu kuwuka kwa akufa.

Yohane 1:29 M'mawa mwake Yohane adawona Yesu alinkudza kwa iye, nanena, 'Onani Mwana wa Nkhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo lake la dziko lapansi!'

Tsamba 42 ndi 43

1Petro 1:19 Koma ndi mwazi wa mtengo wake wapatali monga wa mwana wa nkhosa wopanda chilema, ndi wopanda banga, ndiwo mwazi wa Khristu.

1Akorinto 5:7 ... Pakuti Khristu Pasakha wathu waperekedwa chifukwa cha ife.

2Akorinto 5:21 Ameneyo sadadziwa uchimo adamesera uchimo m'malo mwathu: kuti ife tikhale chilungamo cha Mulungu mwa lye.

Aroma 3:25 Amene Mulungu adamuyika poyera akhale chotetezera mwa chikhulupiro cha m'mwazi wake, kuti awonetse chilungamo chake, popeza Mulungu m'kulekerera kwake adalekerera machimo wochitidwa kale lomwe.

Tsamba 44 ndi 45

Yohane 19:41 - 42 Tsopano pamene lye adapachikidwapo padali munda; ndi m'mundamo mudali manda atsopano m'mene sadayikidwamo munthu aliyense nthawi zonse. Pomwepo ndipo adayika Yesu...

Mateyu 27:62, 65 - 66 Ndipo m'mawa mwake, ndilo dzuwa lotsatana ndi tsiku lokonzekera, ansembe akulu ndi Afarisi adasonkhana kwa Pilato ... 'Tangani alonda; mukani kalondereni monga mudziwa. Ndipo iwo adamuka, nasunga manda, nasindikizapo chizindikiro pamwalapo. Naikapo woyang'anira.

Mateyu 28:2 - 4 Ndipo onani, padali chibvomezi chachikulu; pakuti m'ngelo wa Ambuye adatsika kuchokera Kumwamba nafika kukunkhuniza mwalawo, nakhala pamwamba pake. Kuwonekera kwake kudali ngati mphezi, ndi chobvala chake choyeretsetsa ngati matalala: Ndipo ndikuwopsa kwake alondawo adanthunthumira, nakhala ngati anthu akufa.

Marko 16:6 Ndipo iye adanena nawo, 'musaope: Muli kufuna Yesu Mnazarete amene adapachikidwa; adawuka; Sali pano; tawonani, mbuto m'mene adayikamo lye.'

Tsamba 46 ndi 47

Machitidwe 1:3 Kwa iwonso amene adadziwonetsera yekha wamoyo ndi zitsimikizo zambiri, zitatha zowawa zake, nawonekera kwa iwo masiku makumi anayi, ndi kunena zinthu za Ufumu wa Mulungu.

Yohane 3:16 Pakuti Mulungu adakonda dziko lapansi, koteru kuti adapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wokhulupirira mwa lye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.

Yohane 14:1 - 4 'Mtima wanu usabvutike; mukhulupirira Mulungu, khulupirirani Inenso. M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikudali kutero, ndikadakuwuzani inu; pakuti ndipita kukakonzzerani inu malo. Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso. Ndipo kumene ndipita Ine, mukukudziwa, ndipo njira yake mukuyidziwa.'

Tsamba 48 ndi 49

Machitidwe 1:9 - 11 Ndipo m'mene adanena zinthu izi, ali chipenyere iwo, adanyamulidwa; ndipo mtambo udamlandira lye kumchotsa pamaso pawo. Ndipo pakukhala iwo chipenyere Kumwamba pomuwona lye alimkupita kumwamba, tawonani, amuna awiri wobvala zoyera adayimilira pambali pawo; Amenenso adati; Amuna inu a ku Galileya, muyimiranji ndi kuyang'ana Kumwamba? Yesu amene walandiridwa kumka Kumwamba kuchokera kwa inu, adzabwera momwemo monga mudamuwona ali mkupita Kumwamba.

1Yohane 5:11 - 13 Ndipo uwu ndi umboniwo, kuti Mulungu adatipatsa ife moyo wosatha, ndipo moyo umene uli mwa Mwana wake. Iye wakukhala ndi Mwana ali nawo moyo; wosakhala ndi Mwana wa Mulungu alibe moyo. Zinthu izi ndakulemberani, kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu. Kutu mukhulupirira padzina la mwana wa Mulungu.

Yohane 21:25 Koma palinso zina zambiri zimene Yesu adazichita, zoti zikadalembedwa zonse phe, ndilingalira kuti dziko lapansi silikadakhala nawo malo a mabuku amene akadalembedwa.

Matanthawuzo a Mawu

Ambuye: dzina la Mulungu, kapena la Yesu, pofuna kuwonetsa kuti Iye ndi Mwini wake wa zinthu zonse.

Baibulo: Mawu amenewa amatanthuza buku m'chilankhulo cha Chilatini ndi Chigiriki.

Chilango: mavuto kapena masawutso amene amabwera kwa munthu ngati chotsatira cha tchimo limene wachita.

Chilengedwe: ntchito yimene Mulungu adachita popanga dziko ndi zinthu zonse zimene zili momwemo; zinthu zonse zimene Mulungu adapanga.

Guwa la nsembe: malo a paderadera amene anthu ankawotcherapo nyama imene akufuna kuyipereka nsembe kwa Mulungu.

Khate: matenda woyipa kwambiri. Ndi matenda a khungu ndi mafupa. Anthu ena sankayankhula ndi anthu amene amadwala matenda a khate. Ankawatcha anthu wodetsedwa. Anthu a khate sankakhala mumzinda. Anthu wodwalawa ankakhala kunjira kwa mzinda kutali ndi anthu ena.

Kudalira: kukhulupirira kuti chinthu china chake ndi chowona. Pamene tikhulupirira wina wake.

Kumwamba: malo amene kumakhala Mulungu; malo a chimwemwe ndi mtendere kumene Mulungu amakhala ndipo amachitako ufumu.

Kusamvera: kusamvera.

Lamulo: lamulo limene Mulungu adapereka; malamulo khumi wofunikira kwambiri a Mulungu kapena malamulo amene Mulungu adapereka kwa Mose pa Phiri la Sinai.

M'ngelo: mizimu imene adayilenga kuti izitumikira Mulungu.

Mpulumutsi: Yesu, wotipulumutsa, amene amatilanditsa.

Mtanda: mitengo yiwiri yophatikizidwa. Anthu a ku Roma ankapereka chilango kwa anthu powakhomera pa mtanda kuti afe. Yesu adafa mwa njira imeneyi.

Mzimu: mbali ya munthu imene imakhala ndi moyo pamene thupi lafa; munthu, monga mngelo, mbali yimene yimakhala ndi moyo, ngakhale popanda thupi. Pali mizimu yabwino, monga Mzimu wa Mulungu ndiponso angelo ake. Kulinso mizimu yoyipa, monga Satana ndi angelo ake.

Nthawi zonse/muyaya: nthawi za nthawi; kusakhala ndi mathero.

Nyenga: kuyankhula zinthu zimene sizili zowona kwa anthu ena, kunena bodza.

Satana: dzina la mzimu woyipitsitsa mwa mizimu imene idawukira Mulungu. Iye ali ndi mayina wenanso: Lusifala (nthanda yowala) ndiponso Mdierekezi. Iyeyu ndi mdani wa Mulungu.

Tchimo: kuchita zoyipa, zinthu zoyipa kapena zonyansa; kusamvera Mulungu; kusatsatira malamulo; zinthu zoyipa zimene anthu amachita.

Uthenga Wabwino: Uthenga wabwino wakuti Yesu adabwera kudzatipulumutsa ife; magawo anayi a Buku Lopatulika amene amafotokoza za moyo wa Yesu – Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane.

Woyera: wosiyana ndi wina aliyense, wopatulidwa.

Yahweh: Dzina la Mulungu mchinenero cha Chihebri; nthawi zina amatchedwanso Yehova.

Mawu a wolembe bukuli

1. Chimodzimidzi kunena kuti 'Mulungu ndi wamuyaya'
2. "Wosabwereranso" monga mwa mawu akuti 'muyaya'. Satana amakafika Kumwamba ndi kukaneneza anthu wokhulupirira pamaso pa Mulungu, komabe nthawi zonse sapambana.
3. Baibulo limanena momveka bwino kuti Satana ndi angelo ake sapezeka ku malo atsopanowa, koma kuti kutsogolo kuno adzatsekeredwa kumeneku (Chivumbulutso 20:10)
4. Izi zikhoza kutanthawuza kukhala 'wofanana ndi Mulungu' mnjira yakuti amakhala ndi zinthu zonse zimene zimamupanga kuti akhale Mulungu, kapena 'kufanana ndi Mulungu' pakungokhala 'wodziwa zabwino ndi zoyipa' chabe. Mawu a Mulungu safotokoza ngati Satana adapereka mfundo zokhudzana ndi yesero lakufuna 'kukhala wofanana ndi Mulungu' kapena ngati bodza lake lidangokhala lokhudzana ndi 'kufanana ndi Mulungu' m'dera limodzi lokha ('kukhala wofanana ndi Mulungu

pankhani yakudziwa zoyipa ndi zabwino'). Popeza kuyesera kufotokoza nkhani ya kukhala 'wofanana ndi Mulungu pomadziwa zabwino ndi zoyipa' kukhoza kufunika kufotokoza zinthu ngakhale zosafunikira zomwe zokhudzana ndi nkhanayi, tidangosiya kuti aliyense akhoza kuganiza zimene Satana amatanthawuza. Komabe, chodziwika ndichakuti lidali bodza.

5. 'Pamene afa' zimangotantawuza nkhani ya chiphunzitso cha Mawu a Mulungu chimene chimatchedwa 'kulungamitsidwa.' Phunziro la 'kulungamitsidwa' limafukula zambiri. Ife tikakhala moyo wodalira Ambuye ngati Mpulumutsi wathu, nthawi yomweyo Mulungu amayikiza chilungamo, ndiponso amatiwona ife ngati anthu angwiro ngakhale mmoyo uno. Popeza ndikovuta kuti timvetsetse mmene tikhoza kuyesedwa 'wangwiro' ndi Mulungu pamene tikudziwa kuti tikadali anthu 'woyipa', tangoyesera kutengako mbali yimodzi ya chiphunzitso chimenechi.

Copyrights

GOODSEED® ndi bungwe limene cholinga chake ndi chakuti: *Tikufuna tifotokozere uthenga wa m'Baibulo momveka bwino*. Inutu mukhoza kulunikizana nafe, ngati muli ndi chidwi pa ntchito zimene timachita kapena kumasulira mabuku mzinenero zina.

KHISIMISI NDI NYENGO YA PASAKA - ZITANTHAUZA CHIYANI?

Kusindikizidwa koyamba

Lolembedwa ndi John R. Cross
Zithunzi zidajambulidwa ndi Matt Almy
Lomasuliridwa m'Chichewa ndi Rodrick Banda

ISBN: 978-1-927429-40-2

Copyright © 2010 by GOODSEED® International

What Are Christmas & Easter All About?
Translated from English Edition 3

All rights reserved. No portion of this book may be reproduced in any form without the written permission of the copyright holder. GOODSEED, www.goodseed.com, 'GOODSEED,' and the Book/Leaf design mark are trademarks of GOODSEED International.

Bukuli ndi la Good Seed International. Simulolelwa kusintha bukuli mwanjira ina iliyonse popanda chilolezo cha eni bukuli. GOODSEED, www.goodseed.com, 'GOODSEED,' komanso zizindikiro za bukuli ndi masamba ake onse ndi za GOODSEED International.

Printed in Malawi — Losindikizidwa m'Malawi

201310-170-2000
Chichewa

GOODSEED® International

P. O. Box 3704 • Olds, AB T4H 1P5 • CANADA

Business: 403 556-9955

Facsimile: 403 556-9950

Email: info@goodseed.com

M'mene mungatipezere ku Malawi:

GOODSEED® International

C/O WHEAMS

P.O. Box 31713, Lilongwe 3, Malawi

Mobile: +265 888823400/+265996160444

| | |
|------------------|----------------------|
| Australia | 1800 89-7333 |
| Canada (English) | 800 442-7333 |
| (French) | 888 314-3623 |
| Europe | info.eu@goodseed.com |
| United Kingdom | 0800 073-6340 |
| USA | 888 654-7333 |

www.goodseed.com

KODI BUKU ILI LIKUKAMBA ZA CHIYANI?

Cholinga cha bukuli ndi chakuti lifotokoze kufunika kwake kwa nkhani yofunikira kwambiri imene imapezeka M' buku Lopatulika. Ntchito yanga ndikuyesetsa kufotokoza nkhanayi momveka bwino.

Bukuli lidalembedwa pogwiritsa ntchito mawu osavuta ndi cholinga chakuti munthu aliyense akhoza kulimvetsetsa. Ngati mumavutika kumvetsetsa nkhani zolembedwa movuta, buku ili ndi thandizo lanu. Mau ena amene alembedwa mopingasa ngati (inu) afotokozeredwa pa tsamba 63.

John R. Cross ndi mkulu wolembe mabuku ndipo kwawo ndi ku Canada.
Matt Almy ndi mkulu waluso wa ku America.
Rodrick Banda ndi womasulira wa ku Malawi.

ISBN 978-1-77304-019-6



CNE Chichewa


goodseed
see · hear · understand